# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

**NYENGO MSABATAYI**

**KUYAMBIRA PA 11 MPAKA 17 MARCH, 2024**


## NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Kuyambira mawa Lolemba pa 10 March kufika Lamulungu pa 17 March 2024, **tiyembekezere nyengo ya mitambo ndi mvula ya mabingu m'madera ambiri yomwe igwe**. Izi zikhale chonchi kamba ka dera lodzetsa mvula lotchedwa ITCZ lomwe lakhazikika pa Malawi. Chiopsezo chakusefukira kwa madzi chikhala chokwera m'madera ena monga m'madera am'mphepete mwa nyanja ya Malawi, komanso m'madera otsika ndi m'malo omwe kumachitika madzi osefukira pafupipafupi. Mphepo yamphamvu ya Mpoto idzayamba kuomba panyanja makamaka Lachiwiri 12 mpaka Lachisanu pa 15 March, ili ndi chenjezo kwa asodzi ndi onse ogwiritsa ntchito nyanja kuti akhale tcheru ndi osamala ndi bwino osalowa pa nyanja m'nyengo ya ulosiwu.

Padakali pano dera lampweya opepuka lomwe lili m'njanya ya m'chere ya India pakati pa dziko la Madagascar ndi Mozambique litha kuchuluka nyonga ndikukhala Namondwe wotchedwa **FILIPO** pakati pa 11 mpaka 12 March 2024. Dera la lampweya opepukali likuyembekezeka kumayenda molungika kudziko la Mozambique kenako lizilowera kumwera kwa dzikoli ndipo litha kubwereranso m'nyanjayi India yi Lachitatu pa 13 March. Namondweyu akafika ku Mozambique akhoza ku kulimbikitsa nyengo ya mphepo yamphamvu komanso mvula m'madera ena akum'mwera kwa Malawi komwe alinso pa chiopsezo cha madzi osefukira monga ku Mulanje, Phalombe, Chiradzulu, Thyolo, Blantyre, Mwanza, Nsanje ndi Chikwawa.

## NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

M'sabatayi kuyambira pa 4 mpaka 10 March mvula yamphamvu inadzetsa madzi osefukira m'madera ambiri mwa nyanja monga ku Nkhotakota ndi Mangochi. Ina mwa mvula yochuluka yomwe inayezedwa inali ku Nkhotakota ndi mlingo wa 125.1mm komanso Chintheche ku Nkhata Bay yamlingo wa 109mm pa 4 March. Mvula yochuluka inayezedwanso pa 5 March ku Neno Boma Agriculture yamlingo wa 73.3mm ndipo ku Chichiri inali yokwana 47.5mm. Ndipo pomaliza pa 6 March ku Mahowe ku Chitipa kunali mvula yambiri ya mlingo wa 75.4mm motsatana ndi Njolomole ku Ntcheu yamlingo wa 64.9mm. Onani mapu pansipa.




*Mapu: Mvula yomwe inayezedwa kuyambira kuyambira pa 4 mpaka 6 March 2024.*

## MALANGIZO M'SABATALI

- Tisaoloke, kapena kuyendetsa galimoto pomwe madzi asefukira kapena akuthamanga kwambiri.
- Nthawi zambiri mvula ya mabingu imabwera ndi mphenzi komanso mphepo ya mkuntho, choncho, tibisale malo otetezeka bwino mvulayi ikamagwa.
- Tikonze ndi kusamalira ngalande zodutsamo madzi kuti tichepetse chiopsezo chakusefukira kwa madzi.

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 10 March, 2024**